

Makolo anga akuti ndidzitolere kaye panopa sindili wokonzeka kukwatira

Date: Wednesday, Safar 11, 1447 3:37 PM

Views: 325

Category: Fiqh > Fiqh An-Nikāh > Achinyamata

Question

Makolo anga akuti ndidzitolere kaye panopa sindili wokonzeka kukwatira

Answer

Kutamandidwa konse ndi kwa Allāh!

Ukwati sichinakhalepo chinthu chotsekereza munthu kuti akwaniritse zokhumba zake, koma m'malo mwake ndi chinthu chomwe chimamuthandizanso iyeyo kuti zokhumba zake zija azikwaniritse mosavuta kudzera mu thandizo la Allāh. Shaytwān ndi amene amawanong'oneza anthu kuti asachite kaye nikāh asanakwaniritse zomwe iwowo akuziona kuti ndi zabwino ndipo m'malo mwake, iyeyu (Shaytwān) amawaitanira ku njira yoipa imene imawagwetsera ambiri mu uchimo. Mutha kuona kuti izi ndi zomwe zachuluka masiku ano pamene mwamuna akuchedwetsa ukwati, kapena makolo kuwaletsa ana awo kuti asakwatire kapena kukwatiwa asanamalize sukulu, kapena asanapeze ntchito; ndipo izi zabweretsa masautso pa achinyamata amene ngakhale achedwetsedwa choncho, zokhumba zawozo sizimakwaniritsidwabe.

Anthu ambiri amayesa kuti nikāh imafunikira kukonzekera mokwanira pokhala ndi katundu wambiri komanso chuma. Izi sizoonaka. Rabī' Ibn Ka'b adafotokoza kuti:[1]

بَلَّاقٌ، فَجَّوَزَتِ الْاُةُ عِيْبَرَايَ مَوِيَّاتِ اَدَلَاقَ، مَلَسُو هِلَعِ لَلِصَّيْبِ نَلَّ اْمُدَّحْ اُتُنْكَ
عُيَّ شَلَّتْ مِدْخَ نَعِ يَنْ لَغَشَّيْ نَ اُبْحَا مَوِيَّاتِ اْمُو، اُةُ اْمُو مِيْقِي اْمِ يَدْنَعِ اْمِ هِلَعِ اْوِ هِلَعِ لَلِوُسَرَايَ تُلُقْ
يَفُتُلُقْ مَثْ بَلَّاقٌ، لَلْ دَلَّ شَمُّ هَلْ تُلُقْ، فَجَّوَزَتِ الْاُةُ عِيْبَرَايَ رَخَا اْمُو يَلَّ لَلَّاقْ مَثْ
نَلَّ هِلَعِ اْوِ، يَنْ يَتَرَخَاوِي اَيُّ نُدْرَمَا نَمِ يَنْ حَلَّصِي اْمَبْ مَلَّغَلَّ هِلَعِ لَلِوُسَرَلَّ هِلَعِ اْوِ: يَسْفَن
ةُ شَلَّ اُتَلَّ يَلَّ لَلَّاقَ، مَعَنَّ نَلَّوُقْ اَلَّ شَلَّ اُتَلَّ لَلَّاقَ مَلَسُو هِلَعِ لَلِصَّ هِلَعِ لَلِوُسَرَّ يَلَّ لَلَّاقَ
نَلَّ اُفَلَّ اَلَّ يَلَّ لَلَّاقَ، اَشَّ اْمِ هِلَعِ لَلِوُسَرَّ عَنَّ صِيْلَ تُلُقْ بَلَّاقٌ، فَجَّوَزَتِ الْاُةُ عِيْبَرَايَ
يَنْوُجَّوَزَتْ نَلَّ اْمُكْرُمَايَ وَ اَلَّ سَلَّ اِيْرُقِي يَنْ لَلَّ سَرَّ اَلَّ لَلَّوُسَرَّ: لُقْ - رَا صَنَّا لَنَ مَسَان -
يَنْوُجَّوَزَتْ نَلَّ اْمُكْرُمَايَ مَلَسُو هِلَعِ لَلِصَّ هِلَعِ لَلِوُسَرَّ نَلَّ: تُلُقْ قُ مَثْ يَتَفَّ، اَلَّ اُفَلَّ
لَلَّوُسَرَّ لَلَّوُسَرَّ عَجَّرِي اَلَّ هِلَعِ اْوِ، هِلَعِ لَلِوُسَرَّ لَلَّوُسَرَّ اْوِ اَلَّ اُفَلَّ: اَلَّ اُفَلَّ
يَنْوُجَّوَزَتْ اْوِ يَنْوُجَّوَزَتْ: بَلَّاقٌ، فَجَّوَزَتْ اَلَّ اْمُو يَلَّ لَلَّاقَ.

Ndidali womuthandiza Mtumiki wa Allāh (ﷻ) ndipo tsiku lina adati: “Eh iwe Rabī’! Kodi sungakwatire?” Ine ndidati: ‘Eh iwe Mtumiki wa Allāh (ﷻ)! Ndikulumbira mwa Allāh, ine ndilibe zondiyenereza kuti ndisamalire mkazi komanso sindikukonda kuti china chilichonse chinditangwanitse mu kukusamalira iwe.’ Kenako adandiyankhulanso tsiku lina kuti: “Eh iwe Rabī’! Kodi sungakwatire?” Choncho ndidamuyankha zofanana ndi zimene ndidayankha tsiku loyambalo. Kenako pambuyo pake ndidalingalira mu mtima kuti: ‘Ndikulumbira mwa Allāh kuti Mtumiki wa Allāh (ﷻ) ndi wodziwa bwino zomwe zili zabwino ku umoyo wanga wa padziko pano komanso ku Ākhirah kuposa mwini wakene. Ndikulumbira mwa Allāh! Ngati angandiyankhulenso ine Mtumiki wa Allāh (ﷻ) kachitatu, ndidzamuyankha kuti eya.’ Choncho adandiyankhulanso kachitatu kuti: “Eh iwe Rabī’! Kodi sungakwatire?” Ine ndidati: ‘Amachita Mtumiki wa Allāh (ﷻ) chomwe wafuna (kutanthauza kuti zomwe Mtumiki wa Allāh (ﷻ) amalangiza apa zinali zabwino).’ Apa Mtumiki wa Allāh (ﷻ) adati: “Pita ku banja lakuti-lakuti la anthu achi Ansawārī ndipo ukayankhule (kwa iwowo) kuti: ‘Mtumiki wa Allāh (ﷻ) wanditumiza ine ndipo akukupatsani As-Salām ndipo akukulamulani inu kuti mundikwatitse kwa mkazi wakuti uja.” Iwo adati: ‘Walandiridwa Mtumiki wa Allāh (ﷻ) komanso mtumiki wa Mtumiki wa Allāh (ﷻ). Tikulumbira mwa Allāh kuti sangabwerere mtumiki wa Mtumiki Allāh (ﷻ) tsiku la lero kupatula zokhumba zake zikwaniritsidwe.’ Rabī’ adati: “Choncho adandikwatitsa ndi kundilemekeza.”

Mu hadīth imeneyi tikuphunziramo kuti pamene munthu akuopa kuti akwatire chifukwa cha kupereweredwa, iyeyu aganizire za Allāh Yemwe ali wosamalira akapolo Ake. ‘Abdullāh Ibn Mas’ūd adati:[2]

حَالُّ النَّاسِ فِي غَلَا أَوْسَمَ النَّاسِ

“Funanifunani kulemera kudzera mu ukwati.”

Umar Ibnul Khattwāb adati:[2]

مُهْنُ غِيَّاءِ رَقُفٍ أَوْ نُؤْكَيٍّ نِ: يَلَاغَتْ هَلَلُ لَلْأَقْدَقِ وَحَالُّ النَّاسِ فِي غَلَا بُلْطِيَّ أَلْ نَمَّ يَبَجَّعٍ
وَلُضَفَّ نَمُّ هَلَلُ

Amandidabwitsa yemwe safunafuna kulemera kudzera mu ukwati, chikhalirecho Allāh adati: “Ngati ali osauka, Allāh adzawalemeretsa kuchokera mu chuma Chake.”

Mu kuyankhula kwina, ‘Abdullāh Ibn Mas’ūd adati:[3]

حَالُّ النَّاسِ لَوْطٍ يَلَوَّ أَمْوِيَّ أَوْخٍ يَفُتُّ وَمَا يَنْ أَمْلَعُ أَوْ مَائِيَّ أَرَشَعُ أَلْ يَلْجَأُ نَمَّ قَبَّيِّ مَلَّ وَلَّ
نَنْتَفَلَّ أَعْفَاحَ مُتَجَّوَزَتِّلَّ نَهْيَفَ

“Nditati ndatsala ndi masiku khumi mu umoyo wanga, ndipo ndikudziwa kuti pamapeto pa masikuwa ndimwalira, ndipo ndinali ndi kuthekera kuti nditha kukwatira, ndikanakwatira poopa mayesero.”

Uku kudali kumva kwa ma Swahābah pa nkhani ya ukwati. Tsopano lero makolo akuwatsekereza ana kuti asakwatire msanga chifukwa chowaopera umphawi?

Inu akhī kwatirani ndipo makolo anuwo simuwanyoza mukapanga zimenezi. Zindikiraninso izi: 'Ā'ishah akufotokoza kuti Mtumiki wa Allāh (ﷺ) adati:[4]

سُورَةُ الْأَنْعَامِ مكية آياتها ثمانون
سُورَةُ الْأَنْعَامِ نَزَلَتْ فِي الْبَنَاءِ وَالْإِيمَانِ وَتَحْيَا تَمْلِكُ

Aliyense amene wapata chisangalalo cha Allāh kudzera mu kuwakwiitsa anthu, Allāh adzamukwanira ku zomwe anthu angamukonzere. Ndipo yemwe wapata chisangalalo cha anthu kudzera mu kumukwiitsa Allāh, Allāh adzamusiira chilichonse kwa anthuwo.

Pangani zosangalatsa Allāh osati makolo anu amene akutsutsana ndi zomwe Allāh adalamula.

Allāh ndiye Mwini kuzindikira.

[1] Musnad Abī Dāwūd At-Twayālisī, #1269

[2] Tafsīr Al-Qurtwubī, Vol. 12, tsamba 241; komanso Tafsīr Ibn Kathīr, Vol. 6, tsamba 51

[3] Al-Mawsū'al Fiqhiyyah Al-Kawniyyah, Vol. 41, tsamba 214

[4] Sunan At-Tirmidhī, #2414